

# Nozibele ndi Sisi Litatu

Tessa Welch

Wiehan de Jager

Sitwe Benson Mkandawire

3

Chichewa ny



Kalekale, atsikana atatu anayenda kukathyola nkhuni.



Tsikuli linali lakupya ndipo iwo anaganiza kuti akamyaye kumtsinje. Anasowera ndikutaya manzi nakumyaya mumanzi.



Mwazizi, anaona kuti kwafipa. Anathamangila kumunzi.



Pamene anali pafupi na nyumba, Nozibele anaika kwanja yake pakhosi. Anaiwala ndendele mwina mkanda wovala pakhosi. Anapempha anzace kuti abwelele kumtsinje kukatenga ndendele. Koma anzace anati kwafipa kwambiri.



Nozibele anabwelera kumtsinje okha. Anaipeza ndendele nathamangila kunyumba koma anasowa mumudima.



Kuyangana patali, anaona ungwelu ucokela pakanyumba kang'ono. Anathamangilako nagogoda pacitseka.



Anadabwa kuona galu isegula citseko ndiponso inati, “Ufuna cani?” “Ndasowa ndifunako malo kogona” anatelo Nozibele. “Ngena, ngati sungena nizakuluma” Inatelo galu. Nozibele anangena.



Galu inati, “Ndiphikile” “Sininaphikilepo galu mu umoyo wanga” anatelo Nozibele. “Phika, ngati suphika nizakuluma” Inatelo galu. Nozibele anaphika zakudya zagalu.



Galu inati, “Ndikonzele pogona” Nozibele anati, “Sindinakonzelepo galu pogona mu umoyo wanga” “Ndikonzele pogona, ngati sundikonzela ndizakuluma” Inatelo galu. Nozibele anakonza pogona galu.



Masiku yonse, anali kuphikira, kupyangila ndi kuwashila galu. Tsiku lina galu anati, Nozibele, ndizayendera anzanga. Pyanga munyuba, phika zakudya, ndiponso undiwashile zinthu zanga ndikalibe kubwelera.



Pamane galu inacoka cabe, Nozibele anacosa sisi litatu kucoka kumutu wake. Anaika sisi limodzi pansi pa bedi, yimodzi kumbuyo kwa citseko ndi ina mosungila ng'ombe. Ndiponso iye anathamangila kunyumba mwansanga.



Pamene Galu inabwelera, inasakila Nozibele. “Nozibele ulikuti?” Anapunda galu. “Nilikuno kunyansi kwa bedi” Sisi loyamba linayankha. “Nilikuno kumbuyo kwa citseko” Sisi laciwiri linayankha. “Nilikuno kosungila ng’ombe” Sisi lacitatu linayankha.



Gulu inaziwa kuti Nozibele athawa. Gala anathamanga kuyenda kumunzi kwa Nozibele. Koma abale a Nozibele anali kuyembekeza ndi tumitengo tukulutukulu. Galu inabwelela nakuthawa ndiponso ikalibe kuonekelanso kucoka paja.

# Global Storybooks

globalstorybooks.net

## Nozibele ndi Sisi Litatu

Tessa Welch
Wiehan de Jager
Sitwe Benson Mkandawire

CC BY